

# Tigonjetse
# Matenda a Kashembe

**Mau Oyamba**


Matenda a Kashembe akupezekabe m'dziko muno, makamaka m'madera osungira nyama za kutchire monga a Nkhotakota, Kasungu ndi Vwaza. Pafupifupi anthu zana limodzi (100) amagwidwa ndi matendawa chaka chiri chonse. Choncho unduna wa zaumoyo ukulimbikitsa anthu kudziwa zambiri za matendawa komanso kuchitapo kanthu kuti tigonjetse matendawa.

**Kodi matenda a Kashembe ndi Chiyani?**
Matenda a Kashembe ndi matenda amene amayamba pamene munthu walumidwa ndi ntchentche ya kashembe imene ili ndi tizilombo ta matendawa.

**Kodi zizindikiro za matenda a Kashembe ndi ziti?**
- Kutentha thupi
- Kupweteka kwa mutu
- Kufooka kwa thupi
- Kuphwanya kwa thupi
- Kutsika kwa sikelo
- Kuodzera kapena kusinza mowirikiza masana
- Kutopa mwachangu
- Kutupa mwanabere
- Chiwengo pa malo olumidwa



**Kodi matenda a Kashembe amafala bwanji?**
- Matendawa amafala munthu akalumidwa ndi ntchentche ya Kashembe imene ili ndi tizilombo toyambitsa matendawa.
- Matenda a Kashembe amatha kufala pakati pa nyama ndi munthu, nyama ndi nyama kapena pakati pa munthu ndi munthu.



**Kodi pamadutsa nthawi yayitali bwanji kuti munthu ayambe kuonetsa zizindikiro atalumidwa ndi Kashembe?**
- Pamadutsa sabata ziwiri kapena zitatu.

**Kodi munthu angadziwe bwanji kuti akudwala matenda a Kashembe?**
Angadziwe pamene wayezetsa magazi ku chipatala

**Kodi matendawa ali ndi mankhwala?**
- Inde, matendawa ali ndi mankhwala ndipo ndiochizika wodwala akabwera mwamsanga kuchipatala.
- Koma, matendawa amapha mwachangu ukachedwa kupita kuchipatala

**Kodi pali mavuto otani munthu akapanda kulandira thandizo msanga?**

Mavuto omwe angabwere ndi awa:
- Kuyenda movutikira
- Kukomoka
- Kuchepa kwa chilakolako chogonana
- Kusokonekera kwa ubongo
- Kutha kwa magazi
- Kunyentchera
- Imfa

**Kodi matendawa tingawapewe bwanji?**
- Kuvala zovala zokhutala, zazitali zotchinga m'manja ndi miyendo komanso chipewa
- Alendo okayenda ku nkhalango asayende pa galimoto za mpandadenga
- Tisamale komanso tisachotse nsalu za mumisampha yophera Kashembe
- Tisaononge waya otetezera nyama kutuluka mu nkhalango

**Kumbukirani izi**
- Tsatirani njira zopewera matenda a Kashembe kuti inu ndi banja lanu mutetezeke ku matendawa ndi kukhala moyo wathanzi kuti ntchito zanu zachuma zisasokonekere
- Atsogoleri falitsani ndi kulimbikitsa uthenga wa kapewedwe ka matenda a Kashembe
- Atsogoleri limbikitsani anthu amene ali ndi zizindikiro za matenda a Kashembe kupita ku chipatala msanga
- Atsogoleri limbikitsani anthu kukayezetsa matenda a Kashembe pa chipatala chapafupi komanso malo ena amene azilengezedwa akakhazikitsidwa mwapadera
- Asing'anga tumizani msanga anthu amene ali ndi zizindikiro za matenda a kashembe ku chipatala.



Unduna wa zaUmoyo

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo

# Achipatala, yezani matenda a Kashembe kwa odwala onse ochokera m'madera ozungulira nkhalango zotetezedwa kuti athandizidwe moyenerera



DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*

EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration
with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo

# Samalani ndipo musachotse nsalu zophera ntchentche za Kashembe kuti mupewe matenda a Kashembe



DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*

EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo

# Limbikitsani achibale kupita ku chipatala akaona zizindikiro za matenda a Kashembe kuti akathandizidwe moyenera




DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*

EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo

# Asing'anga tumizani msanga anthu amene ali ndi zizindikiro za matenda a Kashembe ku chipatala.




DNDi
Drugs for Neglected Diseases *initiative*


EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba
Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration
with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

# Kafalidwe ka matenda a Kashembe



**Matenda a Kashembe amatha kufala pakati pa munthu ndi munthu, munthu ndi nyama kapena pakati pa nyama ndi nyama. Matendawa amafala munthu akalumidwa ndi kashembe amene ali ndi tizilombo toyambitsa matendawa.**

Unduna wa zaUmoyo

DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*


EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration
with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo



# Mukaona zizindikiro za matenda a Kashembe kayezetseni kuchipatala mwamsanga kuti muthandizidwe chifukwa matendawa ndi oopsa

DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*

EDCTP

HAT-r-ACC

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021

Unduna wa zaUmoyo

# Odwala matenda a Kashembe amaonetsa zina mwa zizindikiro izi



- Kutentha thupi
- Kupweteka kwa mutu
- Kufooka kwa thupi
- Thupi kuphwanya
- Kutsika kwa sikelo
- Kuodzera kapena kusinza mowirikiza masana
- Kutopa mwachangu
- Kutupa mwanabere
- Kuyabwa kwa khungu
- Chiwengo pa malo olumidwa

***Mukaona zina mwa zizindikiro izi pitani kuchipatala msanga***

DNDi Drugs for Neglected Diseases *initiative*

EDCTP

HAT-r-ACC

Moyo ndi mpamba Usamalireni

Produced by Ministry of Health (Health Education Services in collaboration with Trypanosomiasis programme), Malawi- August 2021